


# *KUYAMBA NDI KUTHA KWA NYENGO YA AMITUNDU*

 Usiku wabwino, abwenzi. Ine ndiri woyamikira kwambiri kuti ndiri pano, usikuuno, kachiwiri. Ndinangochoka kuno, kanthawi kapitako. Ine ndikuganiza, tinatuluka cha mma folo koloko. Ndiyeno ine ndimayenera kuti . . . ife tinapita uko kuti tikawaone abwenzi ena ochuluka. Ndipo ndabwerera, maminiti asanu itakwana seveni, ndimangoyenera kuti ndibwerere kuno. Chotero ine ndikukhala ngati ndikusaka mutu, panobe, M'bale Neville.

<sup>2</sup> Koma, tsopano, pali chopempha chimene chapemphedwa kumene, chochokera kwa winawake mu Chattanooga, Tennessee, wokondedwa wina yemwe anali mu ngozi masabata atatu apitawo, ndipo wagona chikomokere, panobe. Ndipo akupempha pemphero kuno, kuchokera kwa mpingo. Ndi . . .

<sup>3</sup> [M'bale Neville ati, “M'bale Bill?”—Mkonzi.] Inde, m'bale? [“Kodi ine ndingapange kulengeza?”] Inu zedi mukhoza. M'bale Neville, ingobwerani. [“Mundikhululukire ine, M'bale Bill.”] Inde, bwana. [“Ine ndinangotsala pang'ono kuiwala. Ine ndinalonjeza kuti ndilengeza usikuuno.” M'bale Neville akulengeza. Malo osajambulidwa pa tepi.]

<sup>4</sup> Ife tinali—ife tinali kuyankhula za Melkizedeki, Yemwe Iye anali, ndipo ife sitinakhala ngati tinatsirizana nacho. Koma mwinamwake, nthawi yotsatira tikadzabwera muno, ife tikhoza kudzayambira kuchokera pamenepo, tikanali mu Bukhu la Ahebri.

<sup>5</sup> Koma, usikuuno, ife titembenuzira ku Bukhu la Daniele. Ndipo inu amene muli ndi Mabaibulo anu, tembenuzirani ku Daniele 12. Ndipo ife tikuti tiwerenge pang'ono kuchokera pamenepo, ndi kuyankhula, mwina, pa ena a Mawu a Mulungu ochokera mu Bukhu la Daniele.

<sup>6</sup> Tsopano, Daniele anali mmodzi wa . . . anali mneneri yemwe anatengedwa kuchokera ku Yerusalemu, kupita ku Babeloni, mu kutengedwera ku Babeloni, ndi Mfumu Nebukadinezara. Iye anali munthu wamng'ono pamene iye ankapita uko ku Babeloni. Uko kunalibe ochuluka a iwo amene anali akugwiritsabe chikhulupiriro chabwino chakale.

<sup>7</sup> Ine ndimamukonda Daniele, chifukwa chake . . . iye anali atalinga icho mu mtima mwake, pamene iye ankapita uko ku Babeloni, kuti iye akanati akakhale ali wokhulupirira, ndipo iye sanali kupita kukadziyipitsa yekha ndi zakudya za mfumu, ndi zina zotero.

8 Tsopano, chinthu chomwe chimene Daniele anali, mneneri kwa Amitundu. Daniele anawuona m'badwo wonse wa Amitundu ukuwuka ndi kugwa. Iye anali mmodzi woyambirira kuti akhale, ife timamutcha, mneneri wa Amitundu. Iye sanali Wamitundu iyemwini. Koma iye anayiona nyengo ya Amitundu, kuchokera koyamba mpaka kotsiriza; mu mutu wa golide, ndi kudzathera mu mapazi a chitsulo ndi dongo.

9 Ndipo pamene anali kumusi uko, akulinga mu mtima wake kuti sakanati adziipitse yekha ndi nyama ya mfumu, ndi zochita za mfumu.

10 Ndipo gulu lina la m'bale, otchedwa Shadireki, Misheki ndi Abedenigo, anali ali uko ndi iwo; amene sanali aneneri, koma okhulupirira. Ndipo iwo, nawonso, analinga mu mtima mwawo. Ndiyeno pamene okhulupirira anai awo amabwera palimodzi, ine ndikanalingalira, mowirikiza ndithu iwo anali ndi misonkhano ya pemphero limodzi.

11 Basi monga ife timachitira, ife timabwera palimodzi chifukwa ife tiri nazo zinthu zofanana. Inu mukudziwa, pali chiphiphiritso chachikale chimene amati, "Mbalame zanthenga zimawulukira limodzi." Ndipo uwo ndi mwambi wakale, kani. Ndipo icho ndi chinthu chabwino kwambiri, nachonso. Mbalame zanthenga zimawulukira limodzi. Kodi sindinu wokondwa chifukwa cha izo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndithudi. Mbalame zanthenga zimawulukira limodzi.

12 Osati kale litali, ine ndinali nditakhala mu msonkhano kumene kunali munthu akukamba chinachake. Ndipo iye anati, "Chabwino . . ." iye anali akuyankhula za miyoyo imene inapita ku ndende, inali mu ndende, imene Yesu anapita ndipo anakailalikira, itachitika imfa Yake. Ndipo munthu uyu yemwe anali kuyankhula, anati, "Chabwino, kodi inu mukuganiza chiyani za izo?"

13 Ndipo m'bale wachikuda anawuka. Iye anati, "Chabwino, ndizo basi zimene Baibulo limanena. 'Iye anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo imene inali mu ndende.'"

Anati, "Kodi inu mukuganiza kuti iyo inali chiyani?"

14 Anati, "Iyo inali 'Miyoyo imene siinalape, mu kupirira-kotalika, mu masiku a Nowa, pamene chombo chinali chikukonzedwa,' basi monga Baibulo linanenera."

15 Iye anati, "Ayi." Anati, "Umenewo ndi mpingo uno, ukulalikira kwa anthu Achipentekoste awo amene ali mu zipembedzo izi ndi chirichonse, kuwabweretsa iwo kuchokera ku ndendezo."

16 Iye anati, "Tsopano, tayang'anani kuno, m'bale." Iye anati, "Chipentekoste sichinatchulidwe nkomwe pamenepo. Iye ananena kuti. Iye anangonena, kuti, 'Iye anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo imene inali mu ndende.'"

Chotero ine ndinati, “Ameni. Ndiko kulondola.”

17 Ndipo mtumiki anayang’ana mopotolokera kwa ine, ndipo anati, “Mbalame za nthenga zimawuluka palimodzi.”

18 Ine ndinati, “Uko nkulondola, abale a Chikhulupiriro chofunika chofanana, kukhulupirira basi chimene Lemba likunena ndicho Choonadi.”

Daniele anali nawo amzake atatu amenewo omwe anali ndi iye.

19 Inu mukudziwa, ndi zabwino, pamene iwe uli kutali ndi kwanu, kuti umupeze wina yemwe ali ndi iwe, wina yemwe angaime ndi iwe, mzako weniweni wabwino. O, mai! Mu maiko achirendo, pamene iwe umupeza wina yemwe akufuna kuti akhale bwanawe wako, ndipo akukukonda iwe ndipo akumaima ndi iwe, ndizo zolemerera kwambiri; makamaka mlendo.

Ndipo abale awa anatengedwera kutali kuchokera ku mzinda wao.

20 Ndipo mzinda wao unawotchedwa. Ndipo zipangizo zawo zonse, ndi zinthu zoyera za Mulungu, zinali zitatengedwera uko ku Babeloni, ndipo zinakaikidwa mu nyumba yosungira ya Mfumu Nebukadenezara, yemwe anali atawatengera iwo kumeneko, mfumu yaikulu, yapamwamba ya Amitundu. Tsopano, ngati-ngati Mulungu analoleza zimenezo, kuti mzinda wawo uwotchedwe, mpingo wawo kuti uwotchedwe, ndi kuwatengera iwo uko mu mzinda, izo zinali chifukwa iwo anali atachoka kwa Mulungu.

21 Koma Iye anali nayebe wokhulupirira yemwe Iye akanakhoza kuyikapo manja Ake, ndi kuti, “Uyu ndi wantchito wanga.”

22 Mulungu nthawizonse wakhala ali nayo mboni, kwina kwake. Iye samadzisiya konse Yekha wopanda mboni. Ziribe kanthu, ndi . . . nthawizina amafika kwa munthu mmodzi yekha, koma Iye nthawizonse amakhala naye winawake yemwe Iye amakhoza kuyikapo manja Ake, ndi kuti, “Uyu ndi wantchito Wanga, ndipo iye azichita monga Ine ndikumuwuzira iye.” Tsopano, ife timazikonda izo.

23 Kuzindikira ndiye, kuti, pamene abale awa anali ali kumeneko, iwo anayikidwa pa mayeso.

24 Chitsanzo chokongola kwambiri cha chimene wokhulupirira wona amafikapo pamene iye wamulandira kwenikweni Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wake. Iye nthawizonse amaikidwa pa mayeso. Satana akanali mu ntchito yoyesa. Ndipo izo zimabwera kokha kuti zikuthandize iwe. Ndi za ubwino wako.

25 “Mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu ayenera kuti ayeseedwe, kulangidwa, kukwapulidwa,” mwa kuyankhula kwina, “kupatsidwa kupumphuntha kwa pang’ono,

kukuwongola bwino. Ndipo ngati Mulungu amatipatsa ife kulanga kwina, ndipo ife nkusakhoza kukupirira iko, ndiye ife timakhala ana apathengo, ndipo osati ana a Mulungu.”

<sup>26</sup> Tsopano, munthu yemwe waika kwenikweni nkhope yake choloza Kumwamba, ziribe kanthu zimene ziti zizichitika pano pa dziko lapansi, iye akanali ndi nkhope yake moloza Kumwamba. Abwenzi ake akhoza kumusiya iye. Banja lake likhoza kumusiya iye. Abusa ake akhoza kumusiya iye. Koma alipo Mmodzi yemwe sangakhoze kumusiya iye; ameneyo ndi Mulungu. Ndipo pamene malingaliro ako apangika! Ine ndimakonda izo.

<sup>27</sup> Daniele anali atawotcha milatho yonse yambuyoy mwake. Iye sanali kulinga zoti abwereremo, kenanso. Iye sanali kuyang’ana njira yake yambuyoy. Iye anali akuyang’ana, kusasamala zinthu izo zimene ziri za mmbuyoy. Iye anakangamirabe wa ku malo a kuyitana kwapamwamba. Ndipo chimene ife tiyenera kuti tizichita. Ndicho chimene Mpingo uyenera kuti uzichita.

<sup>28</sup> Ndipo monga ine ndikuzindikira, ndiye, Mulungu anamulola Satana kuti amupatse iye mayeso. Ndipo, o, iwo anawayesa iwo, ndi moto. Iwo anawayesa iwo, naponso, ndi khola la mikango. Ndipo, nthawi iliyonse, Mulungu anawatulutsamo iwo, oposa agonjetsi.

<sup>29</sup> “Ochuluka ndi mayeso a olungama, koma Mulungu amamupulumutsa iye kwa iwo onse.” Ndi zopambana bwanji izo! Momwe ife tikuyamikirira izo. Mayesero, masautso, zoyesa, zonse zimagwirira ntchito kwa ubwino! Patapita kanthawi, Mulungu amakhoza kuwona ndiye kuti Iye akhoza kuika chidaliro Chake mwa inu, ndiyeno Iye angachitire zinthu zazikulu kwa inu.

<sup>30</sup> Tsopano ife tikuzipeza, ndiye, kuti Daniele anakhala chida mu dzanja la Mulungu, pamene iye anali ali kutali ndi anthu ake omwe, kunja kwa mzinda wake womwe, kutali ndi mpingo wake womwe. Mu dziko lachirendo, Mulungu anamugwiritsa ntchito iye.

<sup>31</sup> Tsopano, iwe ukhoza kukhala kutali ndi chirichonse chomwe iwe ungate ukhale. Iwe ukhoza kukhala kutali ndi okonedwa ako onse, kapena iwe ukhoza kukhala kutali ndi mpingo wako, koma iwe ukhoza kukhalabe chida mu manja a Mulungu. Mulungu akhoza kukugwiritsa ntchito iwe mwa umboni kapena mwa chirichonse chimene Iye angakhumbe kuti akugwiritsire ntchito kwa icho.

<sup>32</sup> Zitsanzo zokongola! Baibulo langokhala lokhomereredwa kwambiri kudzaza ndi zinthu zimenezo, paliponse pamene iwe ungate mbenuze. Kodi inu simumakonda kuwerenga Mawu? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] O, ine ndimangowawerenga Iwo, nthawizina, ndi kukhetsa misonzi.

33 Kuno masiku angapo apitawo, ine ndinali kuwerenga mu chipinda uko, ndipo ine ndinangochita kukhala pansu ndi kumalira monga khanda. Ine ndinadzuka ndipo ndimayenda mozungulira mpando wanga, kuika dzanja langa pa mpando wanga, kuyang'ana pansu pa Baibulo langa kachiwiri; ine ndinangosweka. Ndinapita mozungulira mpando kachiwiri, ndinayang'ana mmbuyo kachiwiri pa ilo. Ine ndinaganiza, “O Mulungu, mkati mmenemo muli Moyo Wamuyaya, kwa mwamuna aliyense kapena akazi amene angayerekeze kuti ayike chidaliro chawo mwa Ilo, ndi kulikhulupirira Ilo.” Moyo Wamuyaya!

34 Ndipo Iye anati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mukuganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi amene amachitira umboni za Ine.” Fufuzani Lemba.

35 “Mawu a Mulungu ndi nyali ya ku mapazi kwathu,” amene ife—imene ife tiyenera kumalondoleredwa nayo, ndiye. Ndi Kuwala kumene kumatsatira njira imene imatitsogolera ife kuchokera ku chigonjetso kupita ku chigonjetso.

36 Tsopano, inu musanati mukhale nacho chigonjetso, payenera kuti pakhale nkhondo. Ndipo ngati palibe nkhondo, palibe zigonjetso. Chotero ife tiyenera kumakhala oyamikira chifukwa cha zinkhondo ndi zoyesa, ndipo ndi Mulungu amene akutipatsa ife mwayi kuti tikhale nazo zigonjetso. O, mai! Kodi izo sizikukupangani inu wabwinoko pang'ono tsopano? Mukuona? Nkhondo imabwera motsatira; winawake kunena chinachake choyipa pa iwe; matenda kubwera kwa iwe. Mwinamwake Mulungu akukupatsa iwe zosautsa zopepuka izo, kuti Iye akhoze kukuchiza iwe ndi kusonyeza kukukonda Kwake kwa iwe, kukulola iwe kuti uwone chimene Iye akutanthauza ndi icho: Iye amakukonda iwe.

37 Nthano yakale ya m'busa imene inkanenedwa uko ku Yerusalemu, mu malo oyera, ya m'busa atanyamula—nkhosa. Ndipo iye anati, “Kodi iwe ukuinyamuliranji iyo?”

Anati, “Iyo ili ndi mwendo wothyoka.”

Anati, “Iyo inachita motani izo; inagwera mu phompho?”

Anati, “Ayi. Ine ndinaithyola mwendo wakewo.”

38 Iye anati, “Bwanji, ndiwe m'busa wankhaza, kuthyola mwendo wa nkhosa imeneyo.”

39 Anati, “Ayi. Ine ndimaikonda iyo.” Ndipo anati, “Iyo inali kupita mosochera, ndipo ine sindikanakhoza kuipanga iyo kuti isamale za ine. Chotero, ine ndinaithyola mwendo wake, chotero ine ndikanakhoza kumaipatsa iyo chisamaliro china chapadera, chotero ndiye iyo ikanati izindikonda ine ndi kumanditsata ine.”

40 Nthawizina, Mulungu amachita kutilola ife kuti tionongeke, pang'ono pokha, mu thanzi, kuti azitipatsa ife chisamaliro chapadera, kuti atitengere ife pa chilolo chake, kuti atilerere

ife mu chifuwa Mwake. Pamene adokotala anati palibe chinthu chingakhoze kuchitidwa; ndiye Iye amatitengera ife mu chifuwa Chake, kuti, “Taona, Ine ndimakukonda iwe. Ine ndikulola iwe kuti uchiritsidwe.” Mukuona? O, kodi izo sizikungopangitsa moyo bwinoko pang’ono? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] O, Iye ndi wamkulu kwambiri! Iye ndi m’busa wododometsa. Sichoncho Iye?

<sup>41</sup> Palibe zodabwitsa Davide anati, “Ambuye ndi m’busa wanga. Ine sindidasowa ayi.” Ndipo momwe Iye amatitsogolera ife cha mphepete mwa madzi odikha; ndipo amabwezeretsa moyo wawo; ndi kusefukiritsa chikho chathu; ndi—ndipo amatidzoza ife mu kukhalapo kwa mdani! Kodi inu munayamba mwadzozedwapo mu kukhalapo kwa mdani wanu? Kumangochitira umboni mpaka chikho chanu chikumangomawira motaikira, inu mukudziwa. Basi ndi kudodometsa kwake iko kuli kuti ukhale wodzozedwa pamene uli mu kukhalapo kwa mdani wako!

<sup>42</sup> Tsopano zindikirani, ndiye, Mulungu anamutenga Mfumu Nebukadinezara ndipo anamupanga iye chida mu dzanja Lake. Ndipo pamene Mfumu Nebukadinezara anafa, iye atakhala nazo... Maudzu atakula, tsitsi lake, longa mkango, kapena longa nthenga za mphungu; ndi zikhadabo zake zonga zikawalesa za mphungu, ndi zina zotero. Ndipo Mulungu anachita kumulola iye kuti adziwe Yemwe anali Mfumu yeniyeni.

<sup>43</sup> Pambuyo pa imfa yake, Beltishazar, mdzukululu wake, analowa mmalo mwa iye. Ndipo, ndiye, iye anali woyipa kwambiri kuposa Mfumu Nebukadinezara. Ndipo usiku wina, uko, iwo anali ndi phwando lalikulu kwambiri. Iwo anaitana onse awo—oweruza milandu awo ndi mabwana onse mmenemo, ku phwando lalikulu kwambiri. Ndipo pamene iwo anali ndi phwando ili, ndipo iwo anali... anapita, ndipo anaitanitsa, ndipo anakatenga zida, zida zopatulika za Mulungu; kungoti amuselewule nazo Mulungu, ndi kumwera vinyo kwa milungu yawo, kugunditsana zikho, pogwiritsa ntchito zida za Ambuye.

<sup>44</sup> Tsopano, munthu amaloledwa kuti ayende patali chotero, koma pali mzere wolekanitsa pakati pa Moyo ndi imfa. Inu musamati muziuwoloka konse umenewo. Mukuona? Inu mukhoza kumapitirira ndi zopusa zanu zazing’ono kwa kanthawi, koma ndi bwino kuti inu muzidziwa pamene mzere uli. Kodi Ambuye anayamba akuimikani inu pa chirichonse? Iye amatitero, tonse ife, kukoka zingwe zoimitsira, kuti “Apo wapitiriza mokwanira tsopano.” Ndiye kuli bwino kuti iwe uziyang’ana zomwe iwe ukuchita, kuchokera apo mpakana, ngati iwe ukuponda mowoloka cha ku mzere umenewo.

<sup>45</sup> Ndipo usiku umenewo, pamene Mulungu anakoka zingwe zoyimitsira pa iye, ndipo iye sanafune kumvera. Anapitabe uko

ndi kukabweretsa zida za Ambuye, anayamba kumwa vinyo, ndi kugunditsana zikho kwa mulungu wawo. Ndiye pamenepo kunabwera dzanja pansu kuchokera Kumwamba, ndipo linalemba pa khoma, “MENE, MENE, TEKELE, UFARISINI.” Kutanthauza, “Inu mwayezedwa mu muyezo, ndipo mwapezeka operewera.” Palibe wina akanakhoza kutanthauzira zimenezo. Awo anali malirime osadziwika.

<sup>46</sup> Ndipo kunali mwamuna kumeneko, anali ndi mphatso ya kutanthauzira, Daniele, chotero iye anabwera kumeneko natanthauzira ndi kuyiwuza mfumu chimene chikanati chichitike. Ndipo, pamenepo, Mulungu analiwononga fuko limenelo, Babeloni.

<sup>47</sup> Pamene, Daniele, pokhala ali kumeneko, iye anawona masomphenya aakulu, ndipo analemba zokhudza iwo, chifukwa cha chithonhozo chachikulu ichi chimene ife tiri nacho lero, kudziwa, ndi kukhazikitsa mu dongosolo, kutha kwa ufumu wa Amitundu.

<sup>48</sup> Zindikirani ungwiwo wake. Ingozimvetsani izo mwatcheru tsopano. Iye anawona, poyamba, fano litaima pa bwalo, pamene iye ankanthauzira loto la mfumu.

<sup>49</sup> Iye anali munthu wauzimu. Iye ankalota maloto, anawona masomphenya, ankanthauzira maloto. Mulungu anali ndi iye, ndipo aliyense ankadziwa zimenezo, nawonso.

<sup>50</sup> Ndipo pamene iye anawona masomphenya, mutu wa golide, ndi chifuwa apa cha siliva, ndi ntchafu za mkuwa, ndi mapazi a chitsulo, zindikirani, ufumu uliwonse unayamba kulimbirapo pang’ono. Ufumu wa Mfumu Nebukadinezara unali mutu wa golide. Iye anautanthauzira iwo, anamuza iye ndendende basi momwe maufumu amenewo akanati adzapambanirane wina ndi umzake mpaka kumapeto. Ndiye zindikirani, kuchokera ku golide, ndi wofewesetsa, siliva ndi wotsatira, ndiye mkuwa ndi wotsatira, kenako chitsulo ndi chotsatira; kulimbira, limbira, kuzizirira, motalikira kutali!

<sup>51</sup> Zindikirani, ndiye, mkati mwa izo zonse, Daniele analiyang’ana fano mpaka Mwala unadulidwa kuchokera mu phiri, umene unadulidwa mopanda manja. Iwo unagudubuzikira pa chifano ndipo unachiswa icho, ndipo unachipanga icho monga tirigu pa bwalo lopunthira lachirimwe, ndipo mphepo inawuuluzapo. “Ndipo Mwalawo unakula nukhala phiri lalikulu limene linaphimba dziko lonse ndi nyanja.” Kumeneko kunali Kudza kwa Ambuye Yesu, kumene tsopano kuli pafupi.

<sup>52</sup> Iye akupitirirabe. Pamene iye anali uko cha ku mtsinje, tsiku lina, iye analowa mu chizimbwizimbwi ndipo anawona masomphenya. Ambiri a iwo anali ndi iye, iwo sanawaone masomphenyawo, pakuti iwo anapatsidwa kwa Daniele yekha. Inu mukuona izo?

53 Winawake akhoza kuima pafupi kumene ndi iwe, ndipo nkumawona zinthu zimene iwe sungakhoze kuziwona, kuti apulumutse moyo wako. Ndiko kulondola. Winawake nati, “Ine sindikukhulupirira izo. Ine sindinawone kanthu.” Chifukwa izo sizinali za iwe kuti uziwone izo.

54 Iwo amene ankapita ndi Paulo, pamene Paulo anakanthidwa nagwa pa kavalo wake ndipo anachita kugwera pa dothi; ndi kugudubuzika, monga izo zinachitikira, pa dothi; palibe aliyense wa iwo analimva phokoso limenelo kapena kuwona masomphenya amenewo. Paulo anawaona Iwo.

55 Panalibe aliyense wa iwo anaiwona nyenyezi imene inadutsa mofufuzira mulimonse, koma amuna anzeru.

56 Zinthu zambiri, mwa njira imeneyo, Mulungu wakonza kuti anthu enaake kuti aziona, ndipo ena sangakhoze kuziona. O, ine ndimakonda izo! Pamene Mulungu, mu nzeru Zake zopandamalire, anakonzeratu, kapena anadziwiratu, kuti zinthu zina zake zidzachitike, izo zikhoza kuchitika kwa munthu atakhala pafupi kumene ndi iwe, ndipo iwe osadziwa kalikonse za izo.

57 Tayang’anani ku Dotani, pamene Eliya anali uko ku Dotani ndipo iwo anali atazunguliridwa konse kumeneko—ndi alendo amene anabwera mmenemo, ankhondo a Asiriya; akumufunafuna Eliya, mneneri. Pakuti pamene, iwo anayamba kuti afufuze, nthawi iliyonse imene Asiriya akanati abwere ku Israeli, kuti adzapange nkondo, bwanji, Aisraeli amakhala atawabisalira iwo.

58 Ndipo chotero mfumu yaku Siriya inawaitanitsa iwo, inati, “Tsopano, dikirani miniti. Ndi ndani ali wa ife, ndipo ndi ndani ali wa Israeli?” Anati, “Winawake mu gulu langa ndi mzondi, yemwe amapita kukawauza Aisraeli basi kumene ife titi tilowereko, pakuti iwo nthawizonse amakhala ali kumeneko akutiyeembekezera ife.”

59 Ndipo munthu mmodzi anali nao uzimu pang’ono pa iye. Iye anati, “Ayi, bambo anga. Koma ndi mneneri Eliya, pakuti iye amadziwa, mu chipinda chake, kumene inu muti mupite kenako.” Amen.

60 O, pamene mphamvu za atomiki zidzayamba kugwedeza, ine ndiri wokondwa kwambiri kuti Mawu a Mulungu atiuza ife koti tidzapiteko. Tithawire ku Thanthwe, Khristu Yesu! Munthu aliyense Mmenemo ali wotetezeka ndi wotchingidwa. Palibe chingakhoze kukupwetekani inu. Palibe mabomba a atomiki, palibe mizinga, palibe chirichonse, chingakhoze kukhudza osungidwa kwa Mulungu; otetezeka, otchingidwa, ozikika. Ndi chiyembekezo chododometsa bwanji chimene ife tiri nacho mwa Khristu Yesu!

61 Zindikirani, uko kunali munthu ali ndi iye. Wantchito wake, mnyamata wauzimu, ankayenda ndipo ankatsanulira madzi pa



manja a mneneri, udindo waukulu umene iye anali nawo. Koma pamene iye anawaona—ankhondo a Asiriya atazungulira konse ku Dotani, anali atatchingidwa konseko, iye anati, “Atate anga, tayang’anani kunja uko! Ndi chiwerengero chachikulu bwanji! Poti, ife tazunguliridwa!”

<sup>62</sup> Tsopano, zimenezo ndi zachibadwa, pamene chirichonse chiwoneka kuti chikulakwika; kulozetsa chala chawo pa iwe, kunena *izi* ndi *izo*; ndipo adokotala kumati iwe sungakhoze kukhala bwino, ndi zina zotero. Ndicho basi chinthu chachibadwa, kuti iwe uganize, “O, mai, awa ndi mapeto!”

<sup>63</sup> Koma Eliya anati, “Alipo ochuluka ali ndi ife kuposa amene ali ndi iwo.”

<sup>64</sup> Tsopano inu mukhoza kulingalira momwe mneneri ameneyo, kapena Gehazi uyo anamvererera, wantchito. Iye anayang’anitsitsa pa iye. Iye anati, “Bwanji, ine sindikumuwona aliyense.”

Iye anati, “Mulungu, tsegulani maso a mnyamata uyu.”

<sup>65</sup> Ndipo mwamsanga pamene Mulungu anachita chinachake! Ndi izi apa. Mvetsani izo. Pamene Mulungu anatsegula kupenya kwake kwauzimu; konse kuzungulira pamenepo, mneneri, kunaima magaleta a Moto ndi Angelo a Moto. Bwanji, iye anawona . . . Bwanji, agaleta a Moto anachulukuka kuposa ankhondo a Asiriya aja, ndi zikwi. Mapiri onse anali pa Moto; Angelo a Moto, akavalo a Moto, agaleta a Moto.

<sup>66</sup> Ndipo Baibulo limati, “Angelo a Mulungu amawazungulira iwo amene amamuopa Iye.”

<sup>67</sup> Mofanana basi usikuuno! Ine ndikudabwa chimene chikanati chichitike ngati munthu pano, usikuuno, akanakhala nayo mphamvu yoti akanthe maso anu, ndi kuti, “Taonani, aima pozungulira kachisi uno usikuuno!” Inu mukanakhoza kukhala membala pano kwa moyo wanu wonse. Zedi. Inde, bwana.

<sup>68</sup> Nthawizina iwe sungakhoze kuziwona Izo ndi maso ako achibadwa, koma iwe ukhoza kumverera kugunda kwa Izo, Chinachake chiri pafupi. Mphamvu yachisanu ndi chimodzi imene imasonyeza kuti Chinachake chiri pafupi.

<sup>69</sup> Muoneni Iye, mmawa uno, akutsegula makutu a ogontha, kupanga opuwala ndi polio kumayenda cha kuno, ngati panalibe kalikonse kolakwika ndi iwo. Ndi chiani icho? Ndi mphamvu yamkati. Ine ndikutanthauza, mphamvu, mphamvu yachisanu ndi chimodzi ndi chikumbumtima, mzimu, kuti Chinachake chiri pafupi. Khalani ndi chikhulupiro mwa Mulungu!

<sup>70</sup> Tsopano, iwo sanatero, iye sanazione Izo, poyamba. Koma, Eliya mwinamwake sanazione Izo, koma iye anapempha kuti maso a mnyamata awone Izo. Koma Elisha ankamverera kuti Iwo anali pamenepo. Amen.

Tomasi, nthawi ina, anati, “Ndiroleni ine ndiyike manja anga mu mbali Yake.”

<sup>71</sup> Yesu anati, “Tsopano iwe ukuona ndi kukhulupirira. Ndi yaikulu bwanji mphoto ya iwo amene sanawone konse panobe, ndipo komabe akukhulupirira.” Amenewo ndi ife usikuuno, kwa aliyense amene ati adzakhulupirire, popanda kuwona.

<sup>72</sup> Ndipo zindikirani. Ndiye Eliya anayenda kupita kumene kuja uko kumene chochitika ichi chinali, ndipo iye ananena kwa iwo. Choyamba, iye anapita kumeneko, ndipo Baibulo limati, “Iye anawakantha iwo khungu.” Khungu; ndipo anayenda kunka kwa iwo komwe. Mmodzi aliyense anali ndi maso openya mwangwiro, monga momwe ine ndikudziwira. Koma Lemba limati, “Iwo anali akhungu.”

<sup>73</sup> Munthu wamng’ono, mausiku angapo apitawo, anati kwa ine, “Ngati inu muli munthu wa Mulungu, ndikantheni ine khungu.”

Ine ndinati, “Ndinu wakhungu kale.” Mukuona? Mukuona? Wakhungu kale!

<sup>74</sup> Zindikirani. Ndipo iye anayenda kupita kumeneko, kumene chochitika chachikulu ichi chinali, chinthu chachikulu ichi chinali. Ndipo iye anati, “Kodi inu mukumufuna Eliya?”

Anati, “Inde.”

<sup>75</sup> Anati, “Bwerani, nditsateni ine. Ine ndikutengerani inu kwa iye kumene.” Eliya ananena izi kwa iwo. Kodi iwo anali akhungu kwa chiyani? Iwo anali akhungu ku choona chakuti ameneyo anali mneneri wa Mulungu. Iwo anali akhungu kwa icho. Ndipo iye anawatsogolera iwo molunjika kumene ku chiwembu, kachiwiri. Anati, “Bwerani, ine ndikakusonyezani inu Eliya,” ndipo uyo anali Eliya akuwatengera iwo kumeneko.”

<sup>76</sup> Ndipo pamene iwo anayang’ana pozungulira, ndipo anapeza kuti iwo anali atazunguliridwa, mowazinga. Mfumu inati, “Bambo anga, kodi ine ndiwakanthe iwo?”

<sup>77</sup> Iye anati, “Kodi inu mungamtenge mkaidi ndi kumukantha iye?” Anati, “Apatсени iwo chinachake choti adye, ndipo muwatumize iwo ku dziko lakwawo.”

<sup>78</sup> Ndi momwe mungathetsere nkhondo. Kodi si kulondola uko? Ndithudi. O, mai! Ngati ife tikanakhoza kokha kutengera mfundo imeneyo, lero, kuti uzimudyetsa mdani wako. “Kuchita zabwino kwa iwo amene achita zoipa kwa iwe.” Amenii.

<sup>79</sup> Kumeneko, tsopano, khungu. Tsopano, Eliya . . . Kapena, ine ndikutanthauza, osati Eliya, tsopano.

<sup>80</sup> Koma, Daniele, Daniele anawoneratu. Iye anali mneneri. Iye anawona kudza kwa Ambuye. Iye anawona nthawi yotsiriza ikudza. Iye anawona Amitundu akuyamba.

<sup>81</sup> Ndipo ngati inu mutazindikira, Amitundu anayamba ndi—kupembedza-mafano. Iwo anali akupembedza fano lalikulu litakhala pa bwalo apo, fano la munthu: Ine ndikukhulupirira, Daniele, mwiniwake. Chifukwa, Mfumu Nebukadinezara anali atamutcha iye “Beltesazar,” amene anali mulungu wake, ndipo iye anayamba kupembedza chifano cha munthu wolungama, woyera. Ndipo Daniele anakana kuchita izo; momwe anachitira—anachitira ana Achihebri, Shadireki, Misheki, ndi Abedenigo.

<sup>82</sup> Ndi momwe izo zinayambitsidwira. Ndipo izo zinatsutsidwa; mutu uja wa golide unayambitsidwa ndi kupembedza-fano, kukakamizidwira kwa izo, ndipo zinatsirizira mu Dzanja lauzimu likulemba chinenero chazimu chimene kumvetisa kwauzimu kokha kukanakhoza kumvetisa izo. Amen.

<sup>83</sup> Umo ndi momwe ufumu wa Amitundu unayambikira, ndipo iwo udzatulukamo mwa njira yomweyo, ndiko kulondola, mwa ntchito zauzimu, kutanthauzira kwauzimu. Inu mukudziwa zomwe ine ndikuzikamba. Kugwira ntchito kwa chazimu, o, momwe ziliri zododometsa! Kodi sindinu okondwa, usikuuno, inu mumakhulupirira mu zauzimu? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inde.

<sup>84</sup> Tsopano, ndiye, atatha masomphenya amenewa, Iye anamusonyeza iye basi kumene mafuko akanati adzakhale atama. Iye anamusonyeza iye momwe kuti uko kunali zaka zochuluka chotero zodaliridwa pa Ayuda apabe. Iye anati, “Mesiya adzadza. Iye adzanenera mu masabata a makumi asanu ndi awiri, zomwe ziri zaka zitatu ndi theka. Mkati mwa izo, Iye adzadulidwa, zimene ziri zaka zisanu ndi ziwiri. Masabata makumi asanu ndi awiri atsimikiziridwa pa anthu ako; zaka zisanu ndi ziwiri za uneneri kwa Ayuda.” Iye anati, “Ndipo Mesiya, Kalonga, adzadza ndipo adzalosera. Mkati mwa masabata asanu ndi awiri, masiku asanu ndi awiri, Iye adzadulidwa. Mu chonyansa, chopangitsa chipasuko, chidzaima mu malo Ake. Ndipo iwo adzaponda pa makoma a Yerusalemu, Amitundu, kwa nthawi, nthawi, ndi kugawaniza kwa nthawi.”

<sup>85</sup> Tsopano, pamene Mesiya anadza, Yesu, Iye analalikira ndendende zaka zitatu ndi theka, ndipo anadulidwa, kwa Nsembe. Zofukiza za pa tsiku zinachotsedwapo. Ndipo chipasuko, themberero lopangitsa chipasuko, usilamu wa ku Omar, waima lero pa malo a kachisi wopatulika. Mzikiti wa Omar waima ndendende pamene kachisi anaima.

<sup>86</sup> Ndipo iye ananena, kuti, “Iwo akanati adzaponde pa makoma a Yerusalemu, pa Yerusalemu, mpaka nyengo ya Amitundu idzakhale itatha. Koma, pa kutha kwa Amitundu, zidzakhala ziripobe zaka zitatu ndi theka, apobe, kwa Ayuda.”

<sup>87</sup> Tsopano zindikirani chimodzi cha zinthu zokhudza kwambiri cha uneneri wa mbiriyakale.

<sup>88</sup> Ine sindikudzinenera kuti ndimadziwa uneneri wa Baibulo. Koma uku kuli monga kuwerenga nyuzipepala; zomveka kwambiri. Ndipo, zimene ife tikuwerenga Pano, ife tikudziwa ndi Choonadi.

<sup>89</sup> Zindikirani, zikwi ziwiri, eya, zaka mazana makumi awiri ndi asanu, Ayuda akhala atabalalika kupita ku fuko lililonse pansu pa Kumwamba. Monga Mulungu anawumitsa mtima wa Farao, kuwaberetsanso iwo; Iye anawumitsa mtima wa Hitler, mtima wa Mussolini, ndi ena otero, mpaka Iye anawathamangitsa iwo abwerere ku Palestina. Kubwereranso, iwo awapanga iwo fuko kachiwiri. Ndipo pa Meyi sikisi, 1947, mbendera ya Chiyuda inakwezedwa pa Israeli, kwa nthawi yoyamba kwa zaka mazana makumi awiri ndi asanu. Mbendera yakale kwambiri mu dziko inakwezedwa kwa nthawi yoyamba mu zaka mazana makumi awiri ndi zisanu. Ndipo Iye anati, mu masiku otsiriza, “Iye akanati adzakweze chizindikiro pa Yerusalemu,” kusonyeza kuti nthawi ili pafupi.

<sup>90</sup> Ndipo zindikirani, kuno osati kale litali, ine ndinawona kanema wauneneri akuseweredwa wochokera kumeneko. Ndipo iwo akuwaberetsa umo Ayuda amenewo, mwa zikwi, pa ndege. Inu mwaziwona izo mu pepala, ndi zina zotero. Magazini a *Look* ndi *Life* akhala akuzilemba izo. Zikwi za Ayuda akubwerera! Ndipo iwo anawafunsa iwo, anati, “Kodi inu mukubwererera chiyani?” Anthu achikulire, olumala, akuwanyamula iwo pa misana yawo, aang’ono awo anali. Anati, “Kodi inu mukubwerera ku dziko lakwanu kuti mukafe?”

Anati, “Ayi. Ife tikubwerera kuti tidzamuwone Mesiya.”

<sup>91</sup> Yesu anati, “Pamene inu mudzawona mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphukira kwake, ndi mitengo ina yonse ikuyamba kuphukira kwake, mudziwe kuti nthawi ili pafupi, kapena chirimwe chiri pafupi, dzinja. Chotero, pamene inu muwona zinthu izi zikufika pochitika, mutukule mitu yanu, chiwombolo chanu chiri kuyandikira.”

<sup>92</sup> Usikuuno, pamene dziko lino liri ngati chisa cha njuchi ndi chikominisi! O, ine ndinali kuyankhula kwa munthu nthawi yapitayo, pa . . .wina wa ulamuliro wapamwamba, ine ndikukhulupirira, amene ine ndikuwadziwa. Ndipo pamene iye amayankhula zinthu zokhudza fuko lino, ndi chikominisi, izo zikanakhoza kukugwedezeni inu mpaka mu maondo anu, kulondola, momwe ilo liri ngati chisa cha njuchi. Palibe kanthu kolimba panonso, osati ngakhale mu dziko lathu lomwe, nkomwe.

<sup>93</sup> Pali chinthu chimodzi chokha cholimba chimene ine ndikuchidziwa kuti chidzaima, ndicho Thanthwe, Yesu Khristu. Ife tikulandira ufumu umene sungakhoze kusunthidwa. Ndipo mu tsiku lino pamene chinthu chirichonse chikugwa, ife tiri nawo maziko okhazikika, Ambuye Yesu Khristu. Bwerani mwa

Ilo, abwenzi. Ndilo powusa mu nthawi ya mkuntho. Ndi chinthu chopambana bwanji!

Iye anawona zonse izi zikufika pochitika.

<sup>94</sup> Ife tikuwaona Ayuda tsopano. Baibulo linanena kuti Yerusalemu. . .Ndipo iye adzaphulika monga duwa. Ndipo momwe iwo alitsiririra dziko limenelo! Ndipo iwo naponso. . . Mneneri anayankhula ndipo anati, “Tsiku limenelo, kuti, madzi azidzabwera kuchokera kumpoto.” Kunali kopanda madzi kumeneko apo, kopanda kasupe kumeneko apo. Koma mu zaka zingapo zapitazi, kuli okukuma amene abwerapo, ndipo atsirira zigwazo. Ndipo kutsirira kwawo ndi kumodzi kwa malo aakulukulu a malimidwe, chifukwa cha kukula kwake, mu dziko.

<sup>95</sup> Ndi mankhwala onse awa ambiri mu Nyanja Yakufa momwe. Muli mankhwala okwanira akupezeka pansu pa iyo, amene chuma chonse cha mdziko sichikanakhoza kuwagula iwo; mankhwala, ureniamu ndi china chirichonse, pansu pomwe pa Nyanja Yakufa, zomwe tsopano ziri za Israeli.

<sup>96</sup> “Mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphukira kwake.” Osati iwo wokha, koma mitengo inayo ikuyamba kuphukira kwake. Achikominisi akuyamba kuphukira. Wotsutsakhristu akuyamba kuphukira.

<sup>97</sup> Ndipo Mpingo wa Mulungu ukuyamba kuphukira. Iwo ukufalikira mu mphamvu Yake kachiwiri. Chimbalinga chinadya gawo la iwo, chirimamine anadya gawo la iwo, mbozi zinadya gawo la iwo, anoni anadya gawo la iwo, koma Mulungu anati, “Iwo udzakhala moyo kachiwiri.” Iwo ukuyamba kuphukira tsopano.

<sup>98</sup> Mitengo ikuyamba kuphukira. Daniele anawoneratu izo, ndipo anasangalala. Tsopano, pa nthawi ino, iye anati, “Ndipo pa nthawi imeneyo. . .” Mutu wa 12.

*Ndipo pa nthawi imeneyo Mikaeli adzaimirira, kalonga wamkulu amene amaimira ana a anthu ako: ndipo pamenepo kudzakhala nthawi ya mavuto, yonga imene siinakhalepo. . .chikhalireni pali fuko ngakhale mpaka ku iyo. . .nthawi: ndipo pa nthawi imeneyo anthu ako adzawomboledwa, mmodzi aliyense yemwe ati adzapezeke atalembedwa mu bukhu.*

<sup>99</sup> O, mai! Kodi sindinu okondwa kuti dzina lanu liri pa Bukhu Lake? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Pamene iye, Daniele, cha apa, anamuona Iye, “Anabwera kwa wa Masiku Amakezana, Yemwe tsitsi lake linali loyera monga ubweya. Ndipo Iye anatsegula Mabuku. Ndipo iwo anaweruzidwa, munthu aliyense, kuchokera mu Mabuku,” Chiweruzo cha Mpando Woyera waukulu.

<sup>100</sup> Tsopano, Daniele akupatsidwa chitsimikizo ichi, ndipo pa mapeto a nyengo ya Amitundu. Mukawerenge . . . Pamene inu mupita kunyumba, ndi mawa, mukawerenge mutu wa 11. Inu mukhoza kuwona momwe mfumu ya kumpoto ikubwerera kumusi, chimene sichiri chinanso koma Russia, akubwera pansu kuti alimbikire kutsutsa iwo, monga kamvuluvulu. Ndipo Nkhondo yaikulu ya Armagedo idzamenyedwa uko komwe pafupi ndi zipata za Yerusalemu. Zindikirani. O, ine ndimazikonda izi!

*. . . ndipo pa nthawi imeneyo anthu ako adzawomboledwa, mmodzi aliyense yemwe ati adzapezeke atalembedwa mu bukhu, bukhu la moyo wa Mwanawankhosa.*

<sup>101</sup> “Mikaeli, kalonga wamkulu, adzaimirira” (kwa chiani?) “anthu ako.” Chabwino.

*Ndipo ambiri a iwo amene agona mu fumbi la dziko lapansi adzauka (liti?) pamene nthawi izi ziti zidzachitike, ndipo ena wa ku moyo wosatha, ndi ena wa ku manyazi ndi kunyozedwa kosatha.*

<sup>102</sup> Basi monga pali Moyo wosatha, kuliponso kupita kosatha. Izo zimatengera momwe iwe umachitira naye Yesu Khristu mu moyo wako. Ngati inu mukumukonda Iye, ndipo mutabadwa kachiwiri, ndipo muli nawo Mzimu Woyera, inu muli nawo Moyo wosatha. Ngati inu mulibe, inu ndi opanda Moyo wosatha. Ngati dzina lanu linalembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, inu muli nawo Moyo wachisavundi. Ngati ilo silinalembedwe Pamenepo, inu simudzati mudzazindikiridwe.

<sup>103</sup> Nchiyani chimenecho? Mauneneri onse awo ali kukwaniritsidwa; chirichonse, mpakana ku nthawi ino yomwe.

<sup>104</sup> Mutu wa golide wapita kale, monga Daniele anati izo zikanadzati, ufumu wa Chibabelonia.

<sup>105</sup> Pambuyo pa uwo, iye anati, akanati adzakhale Amedi ndi Aperezi. Iwo anapambana ufumu wa Chibabelonia.

<sup>106</sup> Ndipo iwo anagwa kale, kwa (ndani?) Agriki, Alexandra Wotchuka.

<sup>107</sup> Ndipo iwo anagwa kale, kwa (ndani?) Aroma. Ndipo Aroma anamwazikirana, ku dziko lonse, Roma wa kummawa ndi wa kumadzulo, miyendo iwiri.

<sup>108</sup> Ndipo iye anati, “Chitsulo ndi dongo zinali ku zala zaku mapazi; zala khumi, maufumu khumi.” Ndipo iye anati izo sizikanati zidasakanizikane. Ndipo iwo akanati adzakwatirane mosakanizikana pakati pa amodzi ndi enawo; Chiroma ndi Chiprotestanti.”

<sup>109</sup> “Ndipo mu tsiku limenelo,” pamene chinthu ichi chidzakhhalapo, “ndiye Mwala unadulidwa kuchokera mu phiri, popanda manja, ndipo unagubuzikira mkati ndipo unachiswa

chinthucho mwa zidutswa.” Ndipo Iwo unatenga malo a chifanocho.

<sup>110</sup> Chotero, abale anga, ife tikukhala ndi mavuto, usikuuno. “Nkhondo, mphekesera za nkhondo; zivomezi mu malo osiyana; kudodometsa kwa nthawi, mkangano pakati pa mafuko.” Ine ndangobwerera kumene kuchokera ku tsidya la nyanja, ndipo ine sindinaliwone fuko koma limene likunjenjemera mu nsapato zawo. Iwo sali kudziwa chimene chiti chichitike kenako.

<sup>111</sup> Koma sitiri ife othokoza, usikuuno, kuti ife tiri kudziwa chimene chiti chichitike kenako! Ambuye Yesu Khristu adzabwera nthawi yachiwiri, mu ulemenero ndi ufumu! Ndipo mwamuna aliyense kapena mkazi yemwe ati adzapezeke atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, adzawuka ndi okonedwa awo, kuti akakomane nawo Ambuye mu mlengalenga. O, ndi chinthu chopambana bwani! Ndicho chifukwa ife timati:

Chiyembekezo chatu sichinamangidwe pa  
china chirichonse  
Kuposa Magazi a Yesu, ndi chilungamo;  
Ponse pozungulira moyo wanga ukupereka  
njira,  
Iye ndi chiyembekezo chatu chonse ndi  
pochirimikira.

<sup>112</sup> “Ndipo pa nthawi imeneyo, Mikaeli adzaima, kalonga wamkulu.” Mikaeli anali Khristu, ndithudi, Yemwe anamenya nkhondo Zaangelo Kumwamba, ndi mdierekezi. Satana ndi Mikaeli anamenya limodzi, kapena anamenyana wina ndi mzake, kani.

<sup>113</sup> Ndipo, tsopano, “Ndipo pa nthawi imeneyo,” iye anati, “onse amene anapezeka atalembedwa mu Bukhu anawomboledwa. Ndi iwo amene anachita mwachilungamo . . .” Penyani pa izi.

*Ndipo iwo amene—ndipo iwo amene ali anzeru  
adzawala monga kuwala kwa thambo; ndi monga . . .  
ndipo iwo amene atembenezira ochuluka ku  
chilungamo monga nyenyezi kwanthawizonse . . .*

<sup>114</sup> Ine ndimayang’ana pa izo, nthawizina, ndipo ine ndimaganiza, abwenzi. Ine ndimapita panja, mmawa. Ine ndimakonda kuwuka molawirira. Kodi inu simumakonda kuwuka molawirira? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>115</sup> Ine ndikukumbukira pamene abale ndi ine tinali mu mapiri. Molawirira kwenikweni mmawa, pafupi folo koloko, ife timakhoza kuwuka. Kuyang’ana, itapachikika mmbuyo uko, ndipo uko kunali nyenyezi ya mmawa. Iko kumakhala kwa mdima weniweni kusanafike basi kufalikira kwa tsiku.

116 Ife tikuwona mdima uli kusionkhana tsopano. Ndi chiyani icho? Ndi Kuwala kukukanikiza mowuthamangitsa mdima. Mmodzi ayenera kuti apereke njira.

117 Zinthu zonse zokwawa zimene zinakhala zikuthamanga kudutsa usiku, pamene dzuwa ilo litulukira, izo zimapita ku mthunzi pamene kuwala kuwala. Usiku ndi mdima... Usiku ndi kuwala sizingakhoze kukhala mu nyumba imodzi. Ndi kapena mdima kapena kuwala. Ndipo kuwala ndi kwamphamvu kwambiri kuposa mdima.

118 Momwemo ali Khristu wamphamvu kwambiri kuposa adani onse a mdziko.

119 Tsopano, ife timaphunzitsidwa ndi azasayansi; pamene kuwala kuyamba kubwera, iko kumaundanitsa mdima. Ndipo mdima umasonkhanitsa khamu lake lonse palimodzi, kuti umenyane ndi kuwala, koma kuwala kumaugonjetsa ndi kumatulukirapo.

120 Ndipo Baibulo linati, mu masiku otsiriza, kuti, "Satana akanadzakhala akupita konsekonse monga mkango wobangula." Iye ali kusionkhanitsa palimodzi, adani ake onse, abwenzi ake onse, adani athu, ndipo akuwasonkhanitsa iwo palimodzi; kuwunjikana pansu pa mutu waukulu, chilemba cha chirombo, mu malo azachipembedzo, chitaganya cha mipingo. Yonse kulumikizana ndi kudzipanga okha bungwe lalikulu, mofanana monga Chikatolika.

121 Ndipo maufumu a dziko ali kudzilumikiza okha palimodzi, ndipo akupanga mutu waukulu kumeneko, mu zandale, zotchedwa chikominisi.

122 Ndipo Kuwala kwa Mulungu kuli kukanikizabe. Ndi chiyani chikuchitika mu nthawi yomweyo, kuti apange izo? Mpingo wa Chikhristu, Mpingo wa Mulungu wamoyo, uli nkudzozedwa. Mphamvu ikubwera kwa Iwo. Iwo uli kulandira Mzimu Woyera.

123 Chaka chatha, mwa a Uthenga wathunthu, munali otembenezidwa milioni zikwi mazana asanu. Kwakukulukulu kumene kwasesa dziko, kwa zaka pambuyo pa zaka. Ife sitiri mmakwalala panonso. Ife tiri pa msewu wa aleluya. Ife sitiri mu mthunzi, panonso. Otembenuka milioni imodzi zikwi mazana asanu mwa malo a Uthenga wathunthu, chaka chatha, anapitirira Chikatolika ndi china chirichonse. O, mai!

124 Ndi chiyani icho? Kuwala kukusionkhana. Misonkhano yaikulu ya machiritso yasetsa dziko. Aleluya! Kulowa mkati, mpaka ku Formosa, misonkhano yamachiritso ili nkuchitika. Kulowa mkati mpaka mu Japan, misonkhano yamachiritso ili kuchitika. Kukwera ku madera achisanu a kumpoto, misonkhano yamachiritso ikuchitika. Kuzungulira dziko, misonkhano yamachiritso! Aleluya! Amuna akulandira Mzimu Woyera, a kulikonse. Ife tiri pa nthawi yotsiriza.



125 Kodi izo zikuchita chiyani? Ndiye mdierekezi akuti, “Tsopano ndi nthawi yanga.” Iye akusonkhanitsa ankhondo ake. Chitaganya cha mipingo kuyesera kuti ayimitse izo, kumati, “Iwo sali kanthu koma gulu la mabokosi aphokoso. Palibe kalikonse kwa iwo. Izo zonse ndi zotentheka. Palibe chinthu chotero chonga kugwira ntchito mu Zauzimu.”

126 Ndipo pa nthawi yomweyo, mutu wa Amerika...gulu la zamankhwala likulemba chidutsa mu pepala, ndipo anati, “Palibe munthu yemwe ali nawo ufulu kuti azibwera mu chipinda cha odwala, kuti adzatumikire kwa anthu, amene samakhulupirira mwa Mulungu Wamphamvuzonse ndi kumulandira Iye monga mthandizi wawo.” *Christian Herald*, powafunsa madokotala mwezi watha, anapereka zolembe zimene ine sindikanakhoza kuzilemba, mwiniwanga, ngati ine ndikanati ndiyesere kubwekerera pa izo. Ndi chiyani icho? Mkati mwa chirichonse, Mulungu adzapangitsa adani Ake kuti achitire umboni kwa ulemerero Wake. Inde, bwana. Dokotala anati, “Ife tikhoza kokha kupereka zothandizira, koma Mulungu ndiye mchiritsi.”

Ine ndinati, “Amuna aakulu amenewo akungofufuza zimene ife gulu la zizete takhala tikuzidziwa nthawi yonseyi.” Ndiko kulondola.

127 Ena a masiku aulemerero awa, inu mudzapeza kuti mulu uwu wa Mphamvu, imene imasintha mahule kukhala madona, ndi zidakhwa kukhala njonda ndi Akhristu, ndi Mphamvu yomweyo imene iti idzawanyamule iwo kuchokera pa dziko lapansi lino ndi kuwatengera iwo Kwawo mu Mkatulo, ku Ulemerero. Izo zikhoza kukhala mochedwa kwambiri; izo zikhoza kukhala mochedwa kwambiri kwa ochuluka.

128 “Pa tsiku limenelo, Mikaeli adzaimira anthu.” Iye sali kuimira mafuko. Iye akuimira anthu. “Ndipo ambiri a iwo amene akugona mu fumbi la dziko lapansi, ena adzawuka wa ku manyazi osatha ndi chinoyo. Koma iwo amene ali anzeru ndipo atambenzira ena ku chilungamo, adzawala monga nyenyezi kwa nthawi za nthawi.” Aleluya!

Hema kapena msasa, chifukwa chiani kuti ine ndizisamala?

Iwo akundimangira ine nyumba yachifumu Kumeneko. (Mudzabwere uko kuti mudzandiwone ine tsiku lina!)

129 Nchiani icho? Ine ndayendapo panja ndi kuyang’ana pa nyenyezi yammawa yaikulu iyo, pamene iyo iyamba kusuntha kutaliko. Kodi nyenyezi ya mmawa imanena chiyani? Nyenyezi ya mmawa imanyezimiritisa kokha kuwala kwapamwamba kwa dzuwa likudza. Ndi kulondola uko? Nyenyezi yammawa, chifukwa chimene iyo ili yowala kwambiri (inu mukudziwa chifukwa chimene izo ziri?), dzuwa liri pafupi kwambiri kwa iyo.

Ilo limakanikizabe. Ndipo nyenyezi yammawa imalengeza kudza kwa dzuwa.

<sup>130</sup> Chabwino, inu nyenyezi zammawa, ndi nthawi yoti mupite mukulengeza Kudza Kwake! Walani, Nyenyezi zammawa! Wukani molawirira! Iyo imati, “Mwana akhala posachedwapa ali pano!”

<sup>131</sup> Pamene ife tipenya ndi kuyiona nyenyezi yammawa iyo, pamene iyo ikunyezimira mu milengalenga, izo zimatanthauza kuti dzuwa liwala posachedwa kwambiri.

<sup>132</sup> Ndipo pamene ife tiwona Nyenyezi za mmawa za Mulungu, zikuwuka ndi kuwala kwa ulemero wa chiwukitsiro cha Yesu Khristu, zimasonyeka kuti Mmodzi wapamwamba uyo akukanikizabe. Kuwala kukusonkhana, koma Nyenyezi yammawa ikufuula, “Dikirani! Sikuli motalika mpaka kucha kwa tsiku.” Dikirani! Sikuli motalika mpaka kucha kwa tsiku. Khalani mukungodikira. Monga Mlongo Murphy ndi iwo anakonda kuimba, “Khalani mukudikira; kucha kwa tsiku kukubwera poschedwa.” Dikirani mpaka iwo... Nyenyezi zammawa ziri kuwalira kwa dziko tsopano, kuliwalitsa dziko, basi kusanayambe kukhala mdima waukulu, ndi bingu lalikulu lochokera Kumwamba, Kudza kwa Ambuye.

Mvetserani mwatcheru tsopano. Tsopano iye anati . . .

<sup>133</sup> Ine ndayang’ana pa nyenyezi ya mmawa, ndipo ine ndimaganiza, “O, nyenyezi ya mmawa!” Ine ndinayang’ana pansi . . .

<sup>134</sup> Tsiku lina, nditaima pamenepo, M’bale Woods ndi ine. Iye anali atangoyambitsa moto, ndipo ife tinali kupita kuti tikapeze kadzutsa. Ndipo ine ndinatembenuka ndipo ndinayang’ana pa nyenyezi yammawa. Ndinayenda kumka kunja uko mu tchire la mkunguza limenelo; ndipo mphepo ikunong’ona podutsa mapaini. Ine ndinaima pamenepo. Ndinamverera bwino, ndikupuma choncho mpweya wabwino, watsopano wammawa; ndipo iko kunali ngati kwachisanu, chisanu chochuluka. Kupita ku khwawa ilo, nditanyamula chidebe cha madzi, amaundana inu musanauke.

<sup>135</sup> Nditaima pamwamba apo, ndinakweza manja anga, kunja uko mu mapaini amenewo. Ine ndinayang’ana pa nyenyezi ya mmawa. Ine ndinaganiza, “O, tayang’anani kuno, chomwe zaka makumi anai ndi zisanu zachita kwa ine.” Ine ndinati, “O, tayang’anani kuno. Ine ndikuchita makwinya. Manja anga akuchita makwinya; tsitsi likuthothoka; mano akupita. O, chomwe zaka makumi anai ndi zisanu zachita kwa ine! Koma,” ine ndinati, “tayang’anani kutaliko, nyenyezi ya mmawa iyo ili basi yokongola ndi yowala monga iyo inali tsiku limene Mulungu, ‘fhuu,’ anayi wuzira iyo kuchokera mmanja Mwake, ndipo anati, ‘Isiyeni iyo iwale!’”

<sup>136</sup> Ndiye ine ndinaganiza za Lemba ili. Ine ndinati, “Koma Mulungu analonjeza, ngati ife tikanati tikhale anzeru ndi kutembenezira ochuluka ku chilungamo, ife tidzawala kuposa nyenyezi kwa nthawizonse.”

<sup>137</sup> Ine ndinaganiza, “Nyenyezi Yammawa, iwe ukuwala tsopano, koma dikira mpaka ife tidzafike Kumeneko! Aleluya! ‘Kuwala moposa nyenyezi kwa nthawizonse!’”

<sup>138</sup> Ndipo ine ndimakhoza kumva mphepo imeneyo ikubwera pansu pa phiri, pafupi kufalikira kwa tsiku, ikunong’ona kupyola mu mapaini amenewo, kumati:

Kuli Dziko kupitirira mtsinje,  
Lomwe ife timalitcha lokoma kwa  
nthawizonse,  
Ndipo ife timangokalifika gombe limenelo  
mwa kupambana kwa chikhulupiriro;  
Mmodzi ndi mmodzi timafika ku zipata,  
Uko kukakhala ndi achisavundi,  
Pamene iwo azikaimbira mabelu agolide awo  
kwa inu ndi ine.

<sup>139</sup> Ndi chinthu chachikulu bwanji! “Iwo amene ali anzeru adzatembenzira ochuluka ku chilungamo, ndipo iwo adzawala kuposa nyenyezi kwa nthawi za nthawi.”

<sup>140</sup> Chotero ndi kusiyana kwanji kumene izo zimapanga, mulimonse? Kodi kadanga kakang’ono aka nkachiyani kuno? Fumbi lakale laling’ono ili la dziko lapansi, mbozi yopanda nsana, kathupi kakang’ono kachivundi kamene kayenera kuvunda ndi kubwera anso ku fumbi, ndipo mphutsi za khungu zidzalidya ilo! O, mai! Ndiroleni ine ndidzawuke ndi zonse zimene ziri mwa ine, ndi kudzawala kwa ulemerero wa Mulungu! Kudzaika pambali cholemetza chirichonse, kuti Mzimu Woyera ungakhoze kutumiza mphamvu Zake ndi ulemerero, kupyolera mu kulalikira kwa Uthenga ndi kuchiritsa kwa odwala, kuti zikatsimikizire Yesu Khristu atawuka kwa akufa. O, mai!

. . . kwa nthawi za nthawi.

*Koma iwe, . . . Daniele, tsekera mawu, ndipo usindikize bukhu, ngakhale mpaka ku nthawi ya mapeto: pakuti ambiri adzathamangira uku ndi uku, ndipo nzeru zidzachuluka.*

*Ndiye ine Daniele ndinawona ndipo ndinayang’ana, ndipo, taonani, apo panaima ena awiri, mmodzi ku mbali iyi ya gombe la mtsinje, ndi mmodzi pa ina . . . mbali ya gombe la mtsinje.*

*Ndipo mmodzi ananena kwa munthu wovala bafuta (Mzimu Woyera), amene anali pa madzi (anthu ndi unyinj) . . .*

<sup>141</sup> Mzimu Woyera pa anthu! O! Aleluya! Mzimu Woyera!

142 Chivumbulutso 15:16 amanena, kuti, “Unyinji ndi makamu. *Madzi* amatanthauza ‘unyinji ndi makamu a anthu.’”

143 “Ndipo pano pali Mmodzi atavala bafuta woyera, akudzigwedeza Yekha chokwera-ndi-chotsika, pa madzi, atakweza manja Ake Kumwamba, analumbira pa Iye amene ali moyo kwa nthawi za nthawi, ‘Pamene zinthu izi zikuchitika, nthawi sidzakhala iliponso!’” Aleluya!

144 “Nthawi sidzakhala iliponso!” Analumbira kuti, pamene ife tikuwona mafuko awa akusweka, ndi zinthu zikuchitika monga choncho, “Chinsinsi cha Mulungu chakwaniritsidwa kale.”

145 Ndi chiyani icho, “Chinsinsi cha Mulungu”? “Mulungu mwa inu, chiyembekezo cha Ulemerero,” chikuwala apo, ubatizo wa Mzimu Woyera!

146 Ndiye Iye anati, “Pamene zinthu ziti zizidzachitika, nthawi sidzakhala iliponso.”

147 “Iwo amene amudziwa Mulungu wawo,” anatero Daniele. “Mu masiku otsiriza, ambiri azidzathamangira uku ndi uko, nzeru zidzacheluka. Koma iwo amene amudziwa Mulungu wao adzachita zochuluka mu masiku otsiriza.”

148 “Iwo adzachita zochuluka.” O, zochuluka za chikhulupiriro zikufalikira, kuzungulira dziko, usikuuno, mobwera bwereza. Konse konse mmafuko, misonkhano yaikulu! Akhangu akupenya. Ogontha akumva. Olumala akuyenda. Anthu amayendedwe onse a moyo akubwera mkati. Iwo ali kulandira Mzimu Woyera; osati kokha osauka ndi opemphetsa, koma amamilioni ndi china chirichonse. Mulungu akuwatenga ndi kuika mwinjiro Wake pa mmodzi aliyense, ndi kuwapatsa iwo zowayitanira ku Mgonero wa Chikwati.

149 Ndipo Wansembe Wamkulu, Melkizedeki, adzabwera tsiku lina. Ndipo ife tidzadya mgonero, katsopano, ndi Iye, mu Ufumu wa Mulungu, limodzi la masiku aakulu awa, aulemerero! O, ine ndiri wokondwa kwambiri, usikuuno, kuti ndiri mu Ufumu! Inde, bwana. Tsiku lina lalikulu, tsiku lina lododometsa, “Nthawi sidzakhala iliponso!”

150 Mukuona, ife tabwera kuchokera ku Muyaya. Ife tinalipo, dziko lisanakhalepo. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Mulungu anamupanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe.

151 “Kodi iwe unali kuti,” Iye ananena ndi Yobu, pamene Yobu ankaganiza kuti anali ndi nzeru zina. Anati, “Unali kuti iwe pamene ine ndinkaika maziko a dziko, ine ndisanalikhazikitse ilo, pamene ana aamuna a Mulungu ankayimba limodzi ndipo nyenyezi za mmawa zinkafuula mwa chisangalalo?”

152 “Nyenyezi za mmawa zinkafuula mwa chisangalalo.” Iwo owalawo ankafuula mwa chisangalalo, pamene iwo anawona kuti tsiku lina iwo akadzavala kachisi wa pano pa dziko lapansi. Ndipo Mfumu Melkizedeki akanadzabwera mwa chilungamo

cha Mulungu, ndi kudzapereka moyo Wake, kuti atiwo mbolere ife kwa Mulungu, kubwerera kachiwiri, ndipo tsopano nyenyezi zowala kwa nthawi za nthawi.

153 “Unali kuti iwe pamene ine ndinkaika maziko a dziko? Fotokoza kumene iwo anamangirizidwirako. Ndiuze ine pamene iwo akuimapo.” Anati, “Dzimange wekha. Ine ndikufuna kuti ndiyankhule ndi iwe ngati mwamuna.” Ndipo Yobu anagwa pa nkhope yake ngati munthu wakufa. Iye sakanakhoza kupirira izo. Mulungu anali pamenepo. Ndi inu pamenepo. “Unali kuti iwe pamene ine ndinkaika maziko a dziko?”

154 Uthenga waulemerero uwu unali utaneneredwa ndi aneneri a Chipangano Chakale. Izo zabwera mmusi kudutsa mibadwo. Izo ziri pano usikuuno. Izo zatsimikiziridwa ndi Mulungu. Iwo wasesa dziko. Iwo ayesera kuti awuzimitse Iwo.

155 Koma yesera kuti uzimitse moto pa tsiku la mphepo, ndi—ndi mitengo yowuma mu nkhalango? Bwanji, iwe sungakhoze kuchita izo. Pamene iwe ukumenya pa iwo mochuluka, ndi pamene iwe ukuwupatsa iwo mphepo yochuluka; ukamawupatsa iwo mphepo yochuluka, iwo uziyaka molimba. Ndi chinthu chokha.

156 Ife tinkakhala ndi moto waung’ono, uko mu mapiri, pamene ine ndinkakonda kuyesa kupangitsa moto kuti uyake molawirira mmawa. Ine ndinkakhoza kutuluka kunja uko ndi kukaponyera nkhu zina pa iwo; unkachita utsi. Ine ndinkadziwa, motsimikiza monga panali utsi pang’ono, panali moto pamenepo penapake. Chinthu chokha chimene ine ndinkachita ndi kutenga chipewa changa ndi kumaukupiza iwo, ndipo iwo potsiriza unkayaka.

157 Ndicho chimene Mpingo ukusowa lero, ndi kukupiza kwina kwa Mphepo ya mkokomo wamphamvu yonga imene inagwa pa Tsiku la Pentekoste, kuti iwukupize Iwo kubwerera mu Chikhulupiriro kachiwiri, kuti amulandire Ambuye Yesu Khristu pa kudza Kwake mu Ulemerero.

158 Tayang’anani pa zizindikiro, zodabwitsa, zinthu zachinsinsi zimene zikuchitika. “Zivomezi mu malo osiyana; mafunde aakulu akugumula gombe,” basi monga Yesu anati zikanati zidzachite, “mitima ya amuna ikulephera; mantha.”

159 Mantha, “O, ndi ndani amene ati aponye bomba la cobalt loyamba? Ndi chiyani chiti chichitike? Mu maora pang’ono dziko lonse lidzakhala litathapo.” Pakuti, ife tidzakhala tiri mu Kukhalapo kwa Mulungu ilo lisanati konse ligwe kuchokera mu ndege. Ndiko kulondola. Kodi icho chidzakhala chiani? Ichosichidzakhala kanthu, koma ife tidzavula mwinjiro wakale uwu wa mnofu.

Iwo udzagwa, ndi kuwuka ndi kutenga mphoto  
yosatha,  
Ndi kufuula pamene tikudutsa kupyola  
mlengalenga,  
“Tsalani bwino, tsalani bwino,” ora lokoma la  
pemphero.

<sup>160</sup> Izo zonse zidzakhala zitatha, ndipo ife tidzapita Kwathu. Kukaliyika thupi lakale ili pansi; kulisinthanitsa ilo ndi korona ndi mwinjiro, kutsidyako, limene liti lisadzazirale nilitha. Kutembenuka kubwerera ku mwamuna wakale, mkazi wakale, kukhala munthu wamng’ono, kumakhala moyo kwanthawi za nthawi, kuwala moposa; ndi chisavundi, kumayenda chokwera-ndi-chotsika misewu ya Ulemerero, mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu Khristu. Anayimba, “Ulemerero kwa Mulungu wa Mmwambamwamba! Iye wachita zinthu zazikulu pakati pathu.”

<sup>161</sup> Pamene ife tiri mu ulendo lero, tiri ndi Mphamvu ya Mulungu ikutsimikizira chirichonse pa dzanja lirilonse, tiyeni tiyang’ane pozungulira ndipo tiwone kumene ife tiri. Tayang’anani pa mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphukira. Tayang’anani pa mitengo ina ikuyamba kuphukira. Tayang’anani pa mafuko akuyamba kuphukira. Tayang’anani pa Mpingo wa Mzimu Woyera ukuyamba kuphukira. Tayang’anani pa Pentekoste akubwereza, kubwereranso, zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa. Aleluya!

Tiyeni ife tipemphere.

<sup>162</sup> Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu usikuuno, chifukwa cha Mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu, chifukwa cha Umunthu Wake wapamwamba waukulu, chifukwa cha kudzoza Kwake kwa Mzimu Woyera. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa kuti Iye ali pano tsopano, wamoyo, wamoyo nthawizonse, akupanga chitetezero pa kuvomereza kwathu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Mphamvu Yake yochiritsa imene inatikhwathula ife ngati ochokera pamoto, Ambuye, munatibweretsa ife kuchokera ku manda, mwatidzutsa ife ndipo mwawonjezera mphamvu zathu, ndipo mwapitatsa ife Mphamvu, kuti ife tikhoze kumapita ndi kumawala kuno mu mdima uwu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi.

<sup>163</sup> Atate, ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse aliyense amene ali wosapulumutsidwa. Adalitseni onse opulumutsidwa. Perekani izi, Atate. Chiritsani odwala onse; tengani ulemerero. Dalitsani kachisi wamng’ono uyu. Adalitseni anthu. Mdalitseni M’bale Neville, m’busa. Mudalitse madikoni onse, matrastii. Perekani izi, Ambuye. Sanjikani manja Anu amachiritso pa iwo. Ndipo ngati mdierekezi abwera mkati ndi kuyambitsa zosiyana pang’ono, muchiritse izo, Ambuye, mwamsanga kumene, ndi Mvunguti waku Giliadi. Perekani izi, Ambuye. Tsanulirani

mafuta odzozera pa iwo. Apangeni iwo odzichepetsa mu mtima, okoma mu moyo. Mulole iwo aziyenda mu masitepe a Ambuye Yesu. Zinthu zathupi zikachitika kwa iwo ndipo iwo akakhala odwala. Mulole Mngelo wa Mulungu aime pafupi, kuti apake Magazi a Yesu. Perekani izi. Chiritsani matenda onse.

<sup>164</sup> Ndithandizeni ine, Ambuye, pamene ine ndikupita kunja kutali mu minda, powona kusowa kwakukulu kumeneko. Kusowa kwake mu tsikuli! Mamilioni amwalira. Zikwi zana makumi anai ndi zinai achikunja anafa lero, opanda kumudziwa Khristu. Ndithandizeni ine, Wokondedwa Mulungu. Tidalitseni ife tonse, limodzi.

<sup>165</sup> Ndipo tsiku lina, mutidzutse ife kuchokera pa dziko lino lapansi, kotaliko, Ambuye, kuti tidzakakhale ndi Inu mu mpandowachifumu Wanu, mu malo a Mmwambamwamba mmwamba kotaliko, mwa Khristu Yesu. Perekani izi, Atate. Mpaka nthawi imeneyo, mulole thanzi ndi nyonga zikhale zathu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

O, ndifuna kumuona Iye, pa nkhope Yake,  
Kuimbako za chisomo Chake chopulumutsa;  
Mmisewu ya Ulemerero ndzakweza mawu;  
Zonse zatha, ndiri Kwathu, mosangalalabe.

Pa kudutsa dzikoli, ndiyimba pakupita,  
Kulozetsa miyoyo ku Kalvare, ku mtsinje  
wofiira,

Mivi imandilasa kunja ndi mkati;  
Ambuye akunditsogolerabe, mwa Iye  
ndipambana.

O, ndifuna kumuona, pa nkhope Yake,  
Kuimbako za chisomo Chake chopulumutsa;  
Mmisewu ya Ulemerero ndzakweza mawu;  
Zonse zatha, ndiri Kwathu, mosangalalabe.

<sup>166</sup> Tsopano mvetserani, mphindi yokha. Ndi angati Achimethodisti amene ali muno? Kwezani mmwamba manja anu, Amethodisti. Ndi angati Achibaptisti amene ali muno? Kwezani mmwamba manja anu. Ndi angati Achipresbateria ali muno? Kwezani mmwamba manja anu. Ndi angati Anazerini ali muno? Kwezani mmwamba manja anu. Ndi angati Achipentekoste ali muno? Kwezani mmwamba manja anu. Ndi angati Achilutera? Kwezani mmwamba manja anu. Chabwino, ife tonse tiri pano. Penyani, gulu lalikulu kwambiri, litasakanizikana, tonse titakhala mu malo amodzi, mu malo a Mmwambamwamba, tikusangalala mu Dalitso.

<sup>167</sup> Tsopano ine ndikufuna Amethodisti kuti agwirane chanza ndi Abaptisti, Abaptisti ndi Achilutera. Tembenukani pozungulira tsopano ndipo mugwirane chanza manja a wina ndi mzake. Ndipo mutembenukire mbali iyi, tsopano, pamene ife tikuyimba iyo.

Kulozetsa miyoyo ku Kalvare, ku mtsinje  
wofiira,  
Mivi imandilasa kunja ndi mkati;  
Ambuye akunditsogolerabe, mwa Iye  
ndipambana.

O, ndifuna kumuona Iye, pa nkhope Yake,  
Kuimbako za chisomo Chake chopulumutsa;  
Mmisewu ya Ulemerero ndzakweza mawu;  
Zonse zatha, ndiri kwathu, mosangalalabe.

<sup>168</sup> Kodi izo sizikukupangitsani inu kumverera bwino? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi izo sizikukupangitsani inu kumverera monga zanu zonse... Ndi Akhristu angati ali muno? Kwezani dzanja lanu. Aliyense amene amakhulupirira Ambuye Yesu Khristu, kwezani mmwamba dzanja lanu. O, mai! Ndi chinthu chodabwitsa bwanji!

<sup>169</sup> Tsopano pamene ife tikusiyana, pamene ife tikupita, ochokera ku makwathu osiyana, tiyeni tizipita ndi pemphero. Tsopano tiyeni tiziyimba nyimbo yathu yabwino, yachikale yobalalikira. Ndi angati akuyidziwa iyo? *Tenga Dzina la Yesu Ndi Iwe*. Aliyense palimodzi tsopano. Tiyeni tiyimbe.

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wosauka ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Litenge, konse upita.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma kwake! (O kukoma kwake!)  
Chiyembekezo cha pansu ndi chimwemwe cha Kumwamba;  
Inde, Dzina lofunika, O kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha pansu ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Mvetserani.

Pa Dzina la Yesu kugwada,  
Kudzilambatitsa pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu tidzamuveka korona,  
O, ulendo wathu ukadzatha.

Dzina lofunika, O kukoma kwake! (O kukoma kwake!)  
Chiyembekezo cha pansu ndi chimwemwe cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, O kukoma kwake!  
Chiyembekezo cha pansu ndi chimwemwe cha Kumwamba.

<sup>170</sup> Pano pali chimene ine ndikufuna kuti inu muchite.



Tengani Dzina la Yesu nawe,  
Chishango kwa adani onse;  
Mayesero akakusonkhanira,  
Puma Dzina loyeralo mpemphero.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma  
kwake!  
Chiyembekezo cha pansi ndi chimwemwe cha  
Kumwamba;  
Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma  
kwake!  
Chiyembekezo cha pansi ndi chimwemwe cha  
Kumwamba.



*KUYAMBA NDI KUTHA KWA NYENGO YA AMITUNDU* CHA55-0109E  
(Beginning And Ending Of The Gentile Dispensation)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingezezi pa Lamlungu usiku, Januwale 9, 1955, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingezezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1999 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1999 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)